

**NDONDOMEKO YOSAMALIRA NKHALANGO YA CHIFWEREKETE I NDI II  
(VFA) YOKONZEDWA NDI ANTHU MIDZI YA CHIFWEREKETE I NDI II  
MOTHANDIZANA NDI ALANGIZI AZA NKHALANGO A:**

**NTCHISI DISTRICT FORESTRY OFFICE  
P.O. BOX 48  
NTCHISI**

**JULY, 2007**

**NDI THANDIZO LOCHOKERA KU IFMSLP**



**MUNTHU WOLUMIKIZANA NAYE**

**MAKILETI KALIRANI  
CHIFWEREKETE I VILLAGE  
GVH CHIFWEREKETE  
TA NTHONDO  
NTCHISI**

**NAMBALA YA FONI : 09241874**

## **UDINDO WOSAMALIRA NKHALANGO**

Ndondomekoyi idzalongosoledwa ndi bungwe la za nkhalango la midzi ya Chifwerekete I ndi II . Bungweli ndilodziwika bwino, lili mwa a Gogochalo Nthondo ndipo linalebetsa mu kawundula wa za nkhalango ku ofesi ya Ntchisi.

## **KUFOTOKOZA ZA MMENE NKHALANGO YA CHIFWEREKETE I NDI II ILILI**

Nkhalango ya Chifwerekete I ndi II ili mkati mwa midzi ya Chifwerekete I ndi II ndipo ndiyotalikira mtunda wa 13km chakumvuma kwa Boma la Ntchisi.

Nkhalangoyi ndiyayikulu pafupifupi 2.7ha ndipo mbali ina kuli mitengo ya masaizi ya mikangala pamene mbali ina kuli ziphukira zokhazokha ndi mitengo ing'onoing'ono yodalidwa. Mitengo yambiri yopezeka mnkhalangoyi ndi ya mombo ndipo mitundu ina ndi ya: mvukwe, mpoza, thombodzi, kamphoni, kanung'unung'u, nsenga, mtondo, mseza, mpsyipsya, kaumbu mkonkhomwala, mavalokalulu, nkulo, mtsiroti, mpandanjovu, kesiyasi. Dothi lopezeka munkhalangoyi ndi la chifulankhululu.

## **MALIRE YA NKHALANGO**

Malire a nkhalango yathu ndiyodziwika bwino chifukwa timalambula mseu kapena dambule kuzungulira nkhalango yathu ndipo mbali zina malire ndi muzigwembe.

## **UMWINI WA NKHALANGO**

Nkhalangoyi eni ake ndife anthu amidzi ya Chifwerekete I ndi II

## **ANTHU WOGWIRITSA NTCHITO NKHALANGOYI**

Ife anthu amwa Chifwerekete I ndi II ndife eni ake oyambirira kugwiritsa ntchito nkhalangoyi komanso ena amadera ena ndiwoloredwa kudzatenga zinthu mnkhalangoyi koma aliyense ayenera atenge chilolezo kwa akomiti.

## **NTCHITO ZA NKHALANGO**

Ndondomekoyi yapangidwa kuti anthu tizitengako zinthu izi: Bowa, mankhwala, zipatso, udzu. Ntchito yina ndiyosamalira ziphukira kuti anthu tizidzatengako milimo, nkhuhi ngakhale matabwa. Ntchito yina ndiyoteteza nthaka kuti isakokoloke komanso kuti zigwembe ziwundirizike.

## **MAPU YA NKHALANGO**

### **ZIGAWO ZA KASAMALIDWE KA NKHALANGO YATHU**

Nkhalango yathu ili ndi zigawo zenizeni ziwiri.

**1. CHIGAWO CHOYAMBA (FMU 1):** Ichi ndi chigawo chimene muli zigwembe ndipo ndi malo oti atetezedwe. Kukula kwa chigawochi ndi pafupifupi 0.7ha

**2. CHIGAWO CHACHIWIRI (FMU 2):** Ichi ndi chigawo chimene ndi malo otsalawo amene muli ziphukira zambiri komanso timitengo ting'onoting'ono ndipo ndi malo amene ayenera kusamariridwa kuti kutsogoloko adzapereke milimo, nkhuhi, ngakhalenso matabwa. Kukula kwa chigawochi ndi pafupifupi 2.0ha.

### **MAPU YA NKHALANGO KUSONYEZA ZIGAWO ZA KASAMALIDWE KAKE**

### **CHOLINGA CHACHIKULU CHA NDONDOMEKO INO**

Kuteteza, kusamalira ziphukira ndikugwiritsa bwino ntchito zinthu zopezeka mmenemo pothandizikira panyumba ndi pochita malonda ndicholinga chotukula miyoyo yathu

### **ZOLINGA ZING'ONOZING'ONO**

- Kusamalira ziphukira ndi timitengo ting'onoting'ono kuti kutsogoloko tidzapezemo milimo, nkhuhi ngakhalenso matabwa
- Kufuna kupezamo Bowa, mankhwala, zipatso, udzu.
- Kufuna kuteteza nthaka kuti isakokoloke komanso kuti zigwembe ziwundirizike.

Cholinga choyamba ndi chachiwiri chikufotokoza za muchigawo chachiwiri (FMU 2) ndipo cholinga chachitatu chikufotokoza za muchigawo choyamba (FMU 1).

## MALAMULO YA KAGWILITSIDWE NTCHITO KA ZINTHU ZA MNKHALANGO

NAMBALA	LAMULO	CHILANGO
1	Munthu asatenge chinthu cha mnkhalango popanda chilolezo.	Wongotenga adzalipila nkhuu ziwili kapena ndalama zokwana MK800.00
2	Banja lililonse liyenera kudzala mitengo yosachepera 50 pa chaka.	Wophwanya lamuloli adzalipira nkhuu ziwiri.
3	Munthu asadyetse ziweto mnkhalango popanda chilolezo.	Wodyetsa popanda chilolezo adzalipira nkhuu imodzi.
4	Munthu asatenthe mnkhalango popanda chilolezo.	Woteroyo adzalipila mbuzi ziwiri kapena ndalama zokwana MK5000.00
5	Munthu akatenga chilolezo chotolela nkhuu atole zouma.	Wolakwila adzalipila nkhuu ziwili kapena MK800.00
6	Munthu asamenye luzi mnkhalango popanda chilolezo.	Woteloyo adzalipila nkhuu ziwili kapena MK800.00
7	Munthu aliyense ayenera kutenga nawo mbali polima msewu wozungulira nkhalango yathu	Wophwanya lamuloli adzaletsedwa kumaliro kapena kulipira nkhuu ziwiri.
8	Aliyense ayenera kutenga nawo mbali pokhazikitsa nazale yamitengo.	Wosatenga nawo mbali adzalipira nkhuu ziwiri kapena kumuletsa kumaliro.
9	Aliyense ayenera kutenga nawo mbali pozimitsa moto olusa mnkhalango.	Wosatenga nawo mbali adzaletsedwa kumaliro kapena kulipira nkhuu ziwiri.
10	Munthu okhala ndi chilolezo chotolela zipatso atole zogwa zokha kapena kupukusa asagwetse mtengo.	Wogwetsa mtengo adzalipila mbuzi imodzi kapena ndalama zokwana MK2500.00
11	Munthu wofuna kuyika ming'oma mnkhalango ayenela kudula chiphaso chokwana MK300.00 pa mng'oma umodzi pachaka	Wophwanya lamuloli adzalipila mbuzi ziwiri
12	Munthu akatenga chilolezo chokapeza mankhwala mnkhalango adzayenela kutengako pang'ono pamtengo	Wophwanya lamuloli adzalandidwa mankhwala komanso adzalipila mbuzi imodzi kapena ndalama zokwana MK2,500.00
13	Munthu asacheke matabwa mnkhalango popanda chilolezo	Wopezeka adzalipila mbuzi ziwiri kapena MK5,000.00
14	Munthu saloledwa kumanga nyumba kapena khola mnkhalango	Wopezeka adzalipila mbuzi ziwili kapena adzalipila ndalama zokwana MK5000.00
15	Munthu saloledwa kulima mnkhalango	Wopezeka adzalipila nkhuu ziwiri
16	Munthu saloledwa kusintha kapena kuchotsa malile ya nkhalango yathu popanda chilolezo	Wopezeka adzalipila nkhuu imodzi kapena MK400.00
17	Munthu aliyense ayenera kutenga nawo mbali potenthera nkhalango yathu	Wosatenga nawo mbali adzaletsedwa kumaliro kapena adzalipira nkhuu ziwiri kapena MK800.00

**DONGOSOLO LA KASAMALIDWE NDI KAGWILITSIDWE NTCHITO KA  
ZINTHU ZA MNKHALANGO  
CHIGAWO CHACHIWIRI ( FMU 2 )**

**Chotengedwa kunkhalango: Bowa**

**Mitundu yake:** Mphofwa chiwere, , chipindi, ndelema,  
manyami,

**Kufunidwa kwake:** Kwambiri.

**Kupezeka kwake:** Pang'ono zedi

**Mavuto :** Umapezeka pang'ono  
Ziweto zimawononga bowa.  
Kusowa kwa mitengo imene imapangitsa  
kuti bowa umere.

Mvula ikapanikiza bowa umawola msanga.

**Njira zosamalira:** Aliyense wokazula bowa azitenga chilolezo kwa akomiti

Wosadyetsa ziweto malo amodzimidzi

Wokazula bowa azitenga potengera asavunge mmasamba

Wosagwetsa mitengo imene imakonda bowa mwachisawawa

Bowa uzizulidwa kuyambira mwezi wa December mpaka April

Chaka chilichonse ndipo uzizulidwa muzigawo zonse mmene  
ukupezeka

**Kuchuluka Kwa bowa**

**Wotengedwa pa chaka:** Munthu akatenga chilolezo azikazula malingana mmene  
Wapezekera.

**Wopereka chilolezo :** Akomiti

**Otenga chilolezo :** Anthu wozungulira Chifwerekete I ndi II ndi ena akwina

**Mtengo wa chiphaso**

**Chozulira bowa :** Eni wake tizitenga mwa ulele koma akwina, azilipira  
ndalama zokwana K50 ngati cholowera  
Osawerengera kuchuluka kwa bowa wotoledwa.

**CHOTENGEDWA KUNKHALANGO: MANKHWALA  
CHIGAWO CHACHIWIRI ( FMU 2 ).**

**Mitundu ya mitengo ya mankhwala:** Chitedzi chamsanga, m’bwazi, msolo, thombodzi wa Sanga, m’bzoli, chisomo, mpandanjovu, Mtukumphako, nafungwe, nkangamila, palijekanthu Ntondo, mseza, mlungalunga, thupa, mkulasinga, Kaweleka, mkumbatira

**Kufunika kwake:** kwambiri.

**Kupezeka kwake:** kwambiri

**Mavuto ake:** moto wolusa umawononga zitsamba zonse  
Kukumba mankhwala mosasamala monga kugwetsa Mitengo  
Kusema mankhwala mtengo wonse  
Kupulula masamba ambiri kumtengo umodzi  
**Kusamala kwake:** kutentha moto munthawi yake udzu usanaumitsitse  
Masamba asapululidwe ambiri kumtengo umodzi  
Osagwetsa mtengo wonse pofuna mankhwala  
Kukumba mankhwala mbali imodzi yamtengo  
Mankhwala adzatengedwa mzigawo zonse za Nkhalango kuyamba Juni mpaka mtsogolo.

**Kuchuluka Kwa mankhwala**

**Otengedwa pachaka:** Mmene apezekera

**Wopereka chilolezo :** Akomiti

**Wolandira chilolezo** Munthu aliyense wofuna kupeza mankhwala

**Mtengo wachilolezo:** Eni ake ulele  
Anthu akwina adzalipira MK250.00  
chipondamthengo.

**CHOTENGEDWA KUNKHALANGO: ZIPATSO  
CHIGAWO CHACHIWIRI ( FMU 2 ).**

<b>Mitundu yamitengo yazipatso:</b>	Msuku, Mngokhomwala, Nthundu, Nthudza, Kasokolowe, Yembe yembe, Mviru, mtowo,
<b>Kufunika kwake;</b>	Kwambiri
<b>Kupezeka kwake:</b>	Kwambiri
<b>Mabvuto ake:</b>	(a). Khwere zimadya zipatso zaziwisi. (b). Moto wolusa umaononga maluwa azipatso ©. Kudula mitengo yazipatso mwachisawawa.
<b>Kasamalidwe kake:</b>	(a). Osagwetsa mtengo potola zipatso. (b). Kutenthera nkhalango panthawi yake. ©. Kupukusa potola zipatso. (d). Kutenga chotengera pokatola zipatso. (e). Aliyense okatola zipatso atenge chilolezo kwa akomiti. (f). Zipatso zidzatoledwa mzingawo zonse za boloko kuyambira Juni mpaka kutsongolo
<b>Kuchuluka Kwa zipatso zotoledwa Pachaka</b>	Munthu akatenga chilolezo atole malinga ndi mene zapezekela
<b>Wopereka chilolezo:</b>	Akomiti
<b>Wolandira Chilolezo:</b>	Aliyense.
<b>Mtengo wachilolezo:</b>	Wakonkuno ulere wakwina MK10.00 yolowera osawerengera kuchuluka kwa zipatso zotoledwa

**NDONDOMEKO YAKAGWILIDWE KA NTCHITO YOSAMALILA NKHALANGO  
YA MUDZI**

<b>NO</b>	<b>NTCHITO</b>	<b>ZIPANGIZO</b>	<b>KALUZELA</b>	<b>WOCHITA</b>	<b>NTHAWI</b>
1	Kukhazikitsa nazale ya mitengo	Machubu, nkhwangwa, makasu, njere ya mitengo, maleki, makeni, zingwe, mapwitika, mafosholo, mawiribala, visikilo.	Nambala ya mbande zomera mmachubu	Akomiti, Anthu, Mafumu	Mwezi wa Juni mpaka Disembala.
2	Kukonza malo yodzalapo mitengo ( kutchetcha, kupima modzakumbamo mavimbo.)	Masilasha, mapwitika, makasu, mapiki, tepi, chikwalapu.	Kukula kwa malo yotchetchedwa ndi yopimidwa	Akomiti, Anthu, Mafumu	Mwezi wa Ogasiti .
3	Kukumba mavimbo,	Makasu, chikwalapu, mapiki.	Nambala ya mavimbo yokumbidwa	Akomiti, Anthu, Mafumu	Seputembala mpaka Okutobala.
4	Kuwundira mavimbo	Makasu.	Nambala ya mavimbo yowundiridwa.	Akomiti, Anthu, Mafumu	Mwezi wa Okutobala kumapeto mpaka Novembala koyambilira.
5	Kudzala mitengo	Mashovelo, ndowa, mawiribala	Nambala ya mitengo yodzalizidwa.	Akomiti, Anthu, Mafumu	Disembala mpaka Januwale.
6	Kulambulira mitengo ying'onoying'ono	Makasu	Nambala ya mitengo yolambulidwa	Akomiti, Anthu, Mafumu	Marichi mpaka Epulo.
7	Kulima dambule kuzungulira nkhalango.	Makasu, zikwanje, ndowa, madzi mareki.	Kukula kwa malo yolambulidwa.	Akomiti, Anthu, Mafumu	Mwezi wa Epulo mpaka Meyi.
8	Kutenthera	Moto, sakali, mapwitika, makeni, madzi, mareki, akantiga, makasu.	Malo yopazidwa ndi moto.	Akomiti, Anthu, Mafumu	Mwezi wa Juni.



9	Kuyendera nkhalango	Makope, zolemba, zikwanje.	Malipoti.	Akomiti, Anthu, Mafumu	Mwezi wa Juni mpaka Meyi chaka china.
10	Kuzula bowa	Ndowa, matumba, dengue	Nambala ya ndowa ndi matumba wozulidwa ndi bowa	Anthu a mmudzi.	Disembala mpaka Epulo.
11	Kumweta udzu	Chisikiro, chikwanje, makasu.	Nambala ya mitolo ya udzu yomwetedwa.	Anthu a mmudzi.	Kuyambira Juni mpaka Seputembala.
12	Kukumba mankhwala.	Makasu, zikwanje, matumba.	Nambala ya zikunje za mankhwala zotengedwa.	Akomiti, Anthu, Mafumu	Juni mpaka Meyi chaka china.
13	Kutola zipatso.	Ndowa, matumba.	Nambala ya ndowa ndi matumba yotoledwa ya zipatso.	Akomiti, Anthu, Mafumu	Juni mpaka Meyi chaka china.
14	Kulemba malipoti ndikupereka koyenerera.	Mapepala, zolemba.	Nambala ya malipoti yolembedwa.	Akomiti.	Juni mpaka Meyi chaka china.
15	Kuchita misonkhano ya za nkhalango.	Mapepala, zolemba.	Nambala ya malipoti yolembedwa.	Akomiti, Anthu, Mafumu	Juni mpaka Meyi chaka china.
16	Kuwunika malamulo	Makope, zolemba, Mapepala, chakudya.	Malipoti.	Akomiti, Anthu, Mafumu	Disembala.

## NDONDOMEKO YOYENDELA KUNKHALANGO

<b>MALO</b>	<b>OCHITA</b>	<b>ZIPANGIZO</b>	<b>NTHAWI</b>
Ku Nansongole	Chifwerekete I ndi anthu awo ndi akomiti	Zikwanje Zolembera Makope	Juni kamodzi pasabata
Ku nkhalawangwe	Chifwerekete II ndi anthu awo ndi akomiti	Zikwanje Zolembera Makope	Juni kamodzi pasabata
Ku nasongole	Chifwerekete II ndi anthu awo ndi akomiti	Zolembera Zikwanje Makope	Julaye kamodzi pasabata
Ku nkhalawangwe	Chifwerekete I ndi anthu awo ndi akomiti	Makope Zolembera Zikwanje	Julaye kamodzi pasabata
Ku nasongole	Chifwerekete II ndi anthu awo ndi akomiti	Zikwanje Makope Zolembera	Ogasiti kamodzi pasabata
Ku nkhalawangwe	Chifwerekete I ndi anthu awo ndi akomiti	Zolembera Zikwanje Makope	Ogasiti kamodzi pasabata
Ku nasongole	Chifwerekete II ndi anthu awo ndi akomiti	Makope Zolembera Zikwanje	Seputembala kamodzi pasabata
Ku nkhalawangwe	Chifwerekete I ndi anthu awo ndi akomiti	Zikwanje Makope Zolembera	Seputembala kamodzi pasabata
Ku nasongole	Chifwerekete II ndi anthu awo ndi akomiti	Zolembera Zikwanje Makope	Okotobala kamodzi pasabata
Ku Nkhalawangwe	Chifwerekete I ndi anthu awo ndi akomiti	Zolembera Zikwanje Makope	Okotobala kamodzi pasabata
Ku nasongole	Chifwerekete II ndi anthu awo ndi akomiti	Zolembera Zikwanje Makope	Novembala kamodzi pasabata
Ku Nkhalawangwe	Chifwerekete I ndi anthu awo ndi akomiti	Zolembera Zikwanje Makope	Novembala kamodzi pasabata
Ku nasongole	Chifwerekete II ndi anthu awo ndi akomiti	Zolembera Zikwanje Makope	Disembala kamodzi pasabata
Ku Nkhalawangwe	Chifwerekete I ndi anthu awo ndi akomiti	Zolembera Zikwanje Makope	Disembala kamodzi pasabata
Ku nasongole	Chifwerekete II ndi	Zolembera	Januwale kamodzi

	anthu awo ndi akomiti	Zikwanje Makope	pasabata
Ku Nkhalawangwe	Chifwerekete I ndi anthu awo ndi akomiti	Zolembera Zikwanje Makope	Januwale kamodzi pasabata
Ku nasongole	Chifwerekete II ndi anthu awo ndi akomiti	Zolembera Zikwanje Makope	Febuluwale kamodzi pasabata
Ku Nkhalawangwe	Chifwerekete I ndi anthu awo ndi akomiti	Zolembera Zikwanje Makope	Febuluwale kamodzi pasabata
Ku nasongole	Chifwerekete II ndi anthu awo ndi akomiti	Zolembera Zikwanje Makope	Malichi kamodzi pasabata
Ku Nkhalawangwe	Chifwerekete I ndi anthu awo ndi akomiti	Zolembera Zikwanje Makope	Malichi kamodzi pasabata
Ku nasongole	Chifwerekete II ndi anthu awo ndi akomiti	Zolembera Zikwanje Makope	Epulo kamodzi pasabata
Ku Nkhalawangwe	Chifwerekete I ndi anthu awo ndi akomiti	Zolembera Zikwanje Makope	Epulo kamodzi pasabata
Ku Nasongole	Chifwerekete II ndi anthu awo ndi akomiti	Zolembera Zikwanje Makope	Meyi kamodzi pasabata
Ku Nkhalawangwe	Chifwerekete I ndi anthu awo ndi akomiti	Zolembera Zikwanje Makope	Meyi kamodzi pasabata

**DONGOSOLO LOCHITILA KALONDOLONDO**

<b>CHOLINGA</b>	<b>ZOMWE TINGADZAYESE</b>	<b>KAYESE DWE</b>	<b>KALOZELA</b>	<b>WOCHITA</b>	<b>ZIPANGIZO</b>	<b>NTHAWI</b>
Kusamalira ziphukira ndi timitengo ting'onoting'ono kuti kutsogoloko tidzapezemo milimo, nkhuni ngakhalenso matabwa.	Kupezeka kwa milimo kuchokera ku ziphukira	Kuwona	Kuchuluka kwa milimo yochokera ku ziphukira.	Akomiti, Mafumu, Anthu.	Zikwanje, masilasha.	Chakachonse.
Kufuna kupezamo Bowa, mankhwala, zipatso, udzu.	Kupezeka kwa bowa, mankhwala, udzu ndi zipatso.	Kuwona.	Nambala ya matumba wotengedwa.	Akomiti, Mafumu, Anthu.	Zikwanje, masilasha matumba.	Chakachonse.
Kufuna kuteteza nthaka kuti isakokoloke komanso kuti zigwembe ziwundirizike.	Kuchepa kwa kukokoloka kwa nthaka.	Kuwona.	Kuwundirizika kwa zigwembe.	Akomiti, Mafumu, Anthu.	Zikwanje, masilasha.	Chakachonse.

**DONGOSOLO LA ZACHUMA**

**Osayina**

**Mkhalapampando ..... Tsiku**

**G.V.H. .... Tsiku**

**Gogo Chalo ..... Tsiku**

**Mlangizi wamkulu wankhalango mboma ..... Tsiku**

## **MALAMULO OYENDETSERA NKHALANGO YA CHIFWEREKETE I NDI 2**

### **CHOLINGA CHAGULU:**

Kusamalira Nkhalango ya Chifwerekete I ndi 2 mothandizana ndi alangizi a zankhalango ndi kugwiritsa bwino ntchito zithu zopezeka mmenemo.

### **MNDANDANDA WAGULU**

Gulu lidzikhala ndi amaudindi khumi (10) monga wapampando ndi wachiwiri wake, mlembi ndi wachiwiri wake, msungi ndi makomiti membala asanu. Mudzikhhalanso mafumu awa: Chifwerekete I, Chifwerekete II.

Mudzikhhalanso anthu onse ozungulira midzi ya Chifwerekete I ndi 2.

### **WAPAMPANDO NDI WACHIWIRI WAKE**

#### **ZOYENEREZA**

- Akhale wachikondi
- Wolimbikira ntchito yankhalango
- Wodziwa kulemba ndi kuwerengera
- Wokhazikika kudera
- Akhale wachilungamo osati wakatangale

#### **NTCHITO ZAWO NDI MAUDINDO AWO**

- Kutsongolera gulu pakagwiridwe kantchito
- Kukhometsa msonkhano
- Kulimbikitsa gulu
- Kuyang'ana mofooka
- Kuonetsetsa kuti malamulo akugwira ntchito

### **MLEMBI NDI WACHIWIRI WAKE**

#### **ZOYENEREZA**

- Akhale wodziwa kulemba ndi kuwerenga
- Akhale wolimbikira ntchito
- Akhale nzika yakudera

#### **NTCHITO NDI MAUDINDO AWO**

- Kulemba makalata wodziwitsa anthu zamsonkhano
- Kulemba ndikusunga zimene akambirana pamsonkhano
- Kulemba katundu wolowa ndi wotuluka
- Kupereka lipoti lazochitika zagulu

## **MSUNGI**

### **ZOMUYENEREZA**

- Akhale ndi chilungamo
- Akhale ndi malo abwino osungira katundu
- Akhale wodziwa kulemba ndi kuwerenga
- Akhale nzika yakudera

### **NTCHITO NDI MAUDINDO AKE**

- Kusunga katundu wagulu
- Kulemba katundu yemwe walandira ndi yemwe watuluka
- Kupereka lipoti wakatundu mmene akugwirira ntchito

### **MAKOMITI MEMBALA (APHIKA NKHANI)**

#### **ZOWAYENEREZA**

- Akhale wodziwa kulankhula
- Akhale nzika yakudera
- Akhale wakhalidwe labwino

### **NTCHITO NDIMAUDINDO AWO**

- Kuweruza milandu
- Kuyang'ana maudindo mmene akugwirira ntchito zawo.
- Kutumikira mugulu

### **NTHAWI YOKHALIRA PAUDUNDO**

- Nthawi imene gulu linagwirizana pamsonkhano wamidzi yonse ya Chifwerekete 1 ndi 2 yoti munthu adzikhala paudindo ndi zaka zitatu (3) basi.
- Kumapeto kwachaka cha chitatu chili chonse mafumu ayenera kuitanitsa msonkhano wa midzi yonse iwiri ndi kupanmgitsa masankho ena ndipo masankho ake adzikhala oponya voti, munthu mmodzi adziponya voti imodzi paudindo ulionse.
- Mafumu ali ndi ufulu opangitsa masankho mwadzidzi ngati udindo wina ulibe munthu kapena ngati komiti yathetsedwa mwadzidzidzi pazifukwa.

### **ZOMWE ZINGAMUCHOTSETSE MUNTHU PAUDINDO**

- Katangale / kuba
- Kusalemekeza anthu

- Osalimbikira ntchito zoikika mudondomeko yosamalira Nkhalango.
- Wankhaza.

#### **MPHAMVU ZA AKOMITI**

- Kumulipitsa munthu olakwa potsata malamulo
- Kulimbikitsa mgwirizano pagulu
- Kulandira dipo la olakwitsa
- Kuonetsetsa kuti anthu akugwira ntchito zoikika mndodomeko yosamalira Nkhalango.

#### **KATHETSEDWE KA KOMITI**

- Pakatha zaka zitatu A mfumu a Chifwerekete 1 ndi 2 adziyitanitsa msonkhano wagulu lonse kumapeto kwachaka chachitatu chili chonse kupangitsa masankho ena.
- Ngati komiti yasokoneza katundu wagulu iyenera ithetsedwe.

#### **ZOMUYENEREZA MUNTHU KUKHALA MEMBALA WACHIFWEREKETE 1 NDI 2**

- Akhale nzika yamderamo
- Osamwa mowa mwauchidakwa
- Wachikondi ndi wosachita katangale.
- Kalowedwe kagulu ndi kaulele

#### **ZOMUCHOTSETSA MUNTHU KUKHALA MEMBALA**

- Wakhalidwe loipa
- Osalimbikira ntchito

#### **UFULU WOCHITA APILO PAMILANDU YOPEZEKA MUGULU**

- Munthu kapena anthu amene apatsidwa chingamulo pa mlandu ali ndi ufulu wokasuma kubwalo lina ngati sanakhutitsidwe motere: poyamba akachoka kwa akomiti akhoza kupita kwa amfumu, kenako kwa a Gulupu, kwa T/A, mpakana ku khoti
- Munthu kapena anthu wolakwirawo akhoza kubwezeretsedwapo ndi amfumu, a Gulupu, a T/A, Khoti ngati awona kuti mpyoyenerera kutero, ngati sipoyenerera adzachotsedwa ndithu mgulu.

#### **NTCHITO ZA GULU LONSE**

- Kugwira ntchito zoyikika mundondomeko yosamalira nkhalango .
- Kuyang'anira Buloko.
- Kupanga ndi kuwunika malamulo yoyendetsera gulu.
- Kusankha anthu woti akhale mmaudindo

#### **MISONKHANO**

- Akomiti adzichita misonkhano kawiri pamwezi ndipo zokambirana ziyambike akafikapo anthu asanu.
- Msonkhano wa gulu lonse udzichitika kamodzi pa mwezi anthu akafikapo makumi awiri( 20 ) zokambirana ziyambike.



**MALAMULO YA KAGWIRITSIDWE NTCHITO KA ZINTHU ZA MNKHALANGO**

<b>NAMBALA</b>	<b>LAMULO</b>	<b>CHILANGO</b>
1	Munthu asatenge chinthu cha mnkhalango popanda chilolezo.	Wongotenga adzalipila nkuku ziwili kapena ndalama zokwana MK800.00
2	Munthu asadyetse ziweto mnkhalango popanda chilolezo.	Wopanda chilolezo adzalipila nkuku imodzi kapena MK400.00
3	Munthu asatenthe mnkhalango popanda chilolezo.	Woteroyo adzalipila mbuzi imodzi kapena ndalama zokwana MK2500.00
4	Munthu akatenga chilolezo chotolela nkuni atole zouma.	Wolakwila adzalipila nkuku ziwili kapena MK800.00
5	Munthu asamenye luzi mnkhalango popanda chilolezo.	Woteloyo adzalipila nkuku ziwili kapena MK800.00
6	Munthu saloledwa kusaka mnkhalango	Woteloyo adzalandidwa zida komanso adzalipila nkuku zisanu ndi imodzi kapena ndalama zokwana MK2400.00
7	Munthu akhala ndi chilolezo chotolela zipatso atole zogwa zokha kapena kupukusa asagwetse mtengo.	Wogwetsa mtengo adzalipila mbuzi imodzi kapena ndalama zokwana MK2500.00
8	Munthu wofuna kufula uchi akhale ndi chilolezo motsogozedwa ndi akomiti ndi alangizi	Wophwanya lamuloli adzalipila mbuzi imodzi kapena ndalama zokwana MK2500.00
9	Munthu wofuna kuyika ming'oma mnkhalango ayenela kudula chiphaso chokwana MK300.00 pa mng'oma umodzi pachaka	Wophwanya lamuloli adzalandidwa ming'oma yake yonse komanso adzalipila ndalama zokwana MK500.00
10	Munthu akatenga chilolezo chokapeza mankhwala mnkhalango adzayenela kutengako pang'ono pamtengo	Wophwanya lamuloli adzalandidwa mankhwala komanso adzalipila mbuzi imodzi kapena ndalama zokwana MK2500.00
11	Munthu saloledwa kumanga nyumba kapena khola mnkhalango	Wopezeka adzalipila mbuzi ziwili kapena adzalipila ndalama zokwana MK5000.00
12	Munthu saloledwa kulima mnkhalango	Wopezeka adzalipila mbuzi ziwili kapena ndalama zokwana MK5000.00
13	Munthu saloledwa kusintha kapena kuchotsa	Wopezeka adzalipila nkuku ziwili

	malile ya Nkhalango popanda chilolezo	kapena MK800.00
14	Munthu aliyense ayenela kutenga nawo mbali pa ntchito zonse zosamalila Nkhalango.	Wosatenga nawo mbali adzalipila nkuku imodzi kapena MK400.00

### **KAYENDETSEDWE KA ZA CHUMA**

- Msungi ndi amene adzisunga ndalama zonse.
- Ndalama zikapezeka, zina zidzikasungidwa ku Banki imene itsegulidwe ndipo wosayinira wake ndi : wapampando, mlembi ndi msungi.

### **KAPEREKEDWE KA MADIPO**

- Munthu amene wapezeka ndi mlandu sadzigwira nawo ntchito mugulu kufikira atalipira mlanduwo.
- Zolipira zonse zidziperekedwa kwa msungi ndipo chikakhala chiweto chidzigulitsidwa ndi akomiti ndipo ndalamazo ziperekedwe kwa msungi.

### **KASUNGIDWE KA MALEKODI**

#### **CHIFWEREKETE YONSE IDAGWIRIZANA KUTI IDZISUNGA MALEKODI MOTERE:**

- Buku la katundu wolowa ndi wotuluka losungidwa ndi msungi
- Buku la malisiti ndi chilolezo losungidwa ndi msungi
- Buku lolebamo ndalama za gulu losungidwa ndi msungi
- Buku lolebamo mayina ya wanthu wokayendera ku nkhalango losungidwa ndi mlembi
- Buku losainamo alendo wodzawona ntchito mmene ikuyendera losungidwa ndi mlembi
- Buku lolebamo chiwerengero cha wanthu a Chifwerekete 1ndi 2 , losungidwa ndi mlembi
- Buku lolebamo zokambirana za pa msonkhano losungidwa ndi mlembi
- Buku la milandu losungidwa ndi mlembi.

### **KAYENDETSEDWE KA ZA NGONGOLE**

- Ndalama za gulu zitha kubwereketsedwa kwa munthu /gulu lofuna kuchita bizinesi koma akhale wa Chifwerekete 1 ndi 2.
- Chiwongola dzanja ndi 25% ndipo munthu ayenera kuyamba kukongola K1000.00 koma ayenera kubweza pakatha mwezi umodzi.

## **KUSASIYANA MUGULU PA CHILICHONSE**

- Padzakhala kufanana pochita zinthu mugulu pakati pa amai ndi abambo kuyambira pogwira ntchito, kasankhidwe ka maudindo komanso kagawanidwe ka phindu.
- Sipadzakhala kukondera mbali pochita zinthu.

## **KUWUNIKANSO MALAMULO**

- Malamulo adzawunikidwa chaka chilichonse
- A mfumu a Chifwerekete 1 ndi 2 adziyitanitsa msonkhano wa gulu lonse kuti malamulo awunikidwe kumapeto kwa chaka chilichonse.

## **KAGAWANIDWE KA PHINDU**

Phindu lopezeka mnkhalango limene tidzigwiritsa ntchito ndi ili:

- Bowa
- Zipatso
- Mankhwala
- Udzu

## **BOWA, ZIPATSO, MANKHWALA, UDZU**

Banja lili lonse lidzikatenga chilolezo mwaulele chokatengera zinthu zimenezi ndipo akwina azilipira motere:

- Bowa ndi K50.00 yolowera
- Zipatso ndi K10.00 yolowera
- Mankhwala ndi K250.00 chipondamthengo
- Matondo ndi K250.00 yolowera
- Udzu ndi K10.00 yolowera

Ndalama zake zidzagwira ntchito ngati zalembedwera ( muntundamo ) pa zankhuni

## **KUYAMBA KUGWIRA NTCHITO KWA MALAMULO**

Malamulo ya Chifwerekete adzayamba kugwira ntchito pa 1<sup>st</sup> Juni, 2008.


**OSAYINIRA**

**WAPAMPANDO.....TSIKU**

**A GULUPU A CHIFWEREKETE..... TSIKU**

**GOGO CHALO NTHONDO ..... TSIKU**

13. SIGNED:

  
J.S. D. KAYAMBA ZINDWA

DIRECTOR OF FORESTRY

Dated... 14/03/2013


AND

Thikoko Mosen

CHAIRPERSON, LOCAL FOREST ORGANISATION

Dated 24/5/2013

WITNESSES:


  
GROUP VILLAGE HEADMAN

CHIEF MTHONDO  
MTHONDO HEADQUARTERS  
MAY 2013  
P.O. BOX 1 NITCHISI

TRADITIONAL AUTHORITY TCHISI

Dated... 24/05/2013

Dated 24/5/2013

  
DISTRICT COMMISSIONER

THE DISTRICT COMMISSIONER  
27 MAY 2013  
P.O. BOX 1, NITCHISI

Dated... 24/05/2013